

Level 2

# Ndasuzira!

Author: Samvida Venkatesh
Illustrator: Sandhya Prabhat
Translator: Agnes N.Singine Nyendwa




Soniya anali wosangalala. Ali ndi zaka zisanu ndi chimodzi lero!
Ababa anali kupanga zakudya zapadera. Anzake okondeka a Soniya - Amini, Zondi, Harriet, Jude, Khadani, Maliya, Puli (amene anali wodzikuza), Rodwelo, ndi Simi - anali kubwera ku madyerero.



Gogodu-gogodu! Anali Maliya. Anabweretsa mphatso yaikulu. Ooooh!
Gogodu-gogodu! Gogodu-gogodu!
Posachedwa, alendo onse asanu ndi anai anafika. Heyaaaaa !







"Tiyeni tisewere kasozo!" ananena Soniya.
Soniya anali kukonda masewera a kasozo chifukwa anali katswiri wodziwa kukhala chete. Nthawi ina, Maliya sanamupeze kufikira ola limodzi.
"Mwini tsiku ayenera kuwerenga!" ananena mokweza mau Puli (amane anali wodzikuza).




Gogodu-gogodu!
Nanga angakhale ndani? Anali atate ake Jude, anaoneka kutchena. anali kuyendetsa magalimoto a hotela yaikulu. Ndaitanidwa kunchito,"  ananena. "Jude afunikira kukalela mlongosi wake. Pepa, Jude. Tsiku la bwino, Soniya."










Jude anapita wosakondwera. Soniyanso sanakondwere. Tsopano alendo akhala asanu ndi atatu ku phwando. "Bwerani! ananena mokweza mau Puli (amene anali wodzikuza). "Tiyeni tiyambe masewera!"
Soniya anamkhwenzulira diso, kenaka anatseka maso nayamba kuwerenga.



"1, 2, 3..."Khadani anadzipomba muphasa.
"4, 5, 6..." Puli anayenda m'chipinda chosungiramo zinthu.
"7,8,9... Harriet anathamangira pabwalo pa chitseko.
"Khumi!" anakuwa Soniya. "Ngakhale simunakonzeke, ine ndibwera!"




Anthu asanu ndi atatu ofunikira kupeza!
Soniya anathamanga mnyumba ngati munthu wofuntha,
ndikuputhwa pa mphasa.
"Awu!"ananena Soniya.
"Awu!" Inanena mphasa.
"Nasuzira Khadani!" anayimba Soniya. Ogo Khadani!
Angati ofunikira kupeza? Asanu ndi awiri!




"HOU HOU HOU!" Galu wa Soniya Banja analowa mnyumba ndi chitambala chofiirira. Zondi analowa mofulumira m'mbuyo mwake.
"Galu woipa!" ananyoza. "
"Galu wosamva!"
"Ndasuzira Zondi!" anaseka Soniya,
Inali yapafupi iyo!
Angati atsala? Asanu ndi m'modzi!



Soniya anathamangira m'chipinda.
Kulibe munthu kumbuyo kwa matilesi.
Mulibe m'kati mwa thiranki.



"YETSEEEEE!" Munayetsemula mu kabati.
Soniya natsekula chitseko. "YETSEEEE!" anayetsemulanso Rodwelo
"Mulifumbi kwambiri muno, anadandaula Amini.
"Ndasuzira Rodwelo ndi Amini" anaomba m'manja Soniya
Angati atsala kuti apezeke? Anai!





Soniya anakwera patsindwi. Chinthu chinasuntha kumbuyo kwa tanki ya madzi. Soniya anakwawira kufupi.
"SSSSSS!" Chona analonthoka, ndikupita panthambo yoyanikapo zobvala,
"Yandaaaaa!" Chobvala cha amai chinakuwa mwamantha ndikugwera pansi mumtolo
"Ndasuzira Simi!" anakondwa Soniya.
Angati atsala?
ATATU!





"SAAAAA! CHOKA APA! AIIIII!"
Nanga ndichiyani chili kuchitika? Soniya anathamangira kumalo ozungulira nyumba.
kumbuyo kwa maluwa, anaona atsikana awiri ali ndi mantha ndi njuchi imodzi yonenepa.
"Ndasuzira Harriet!" anakuwa Soniya, ali kuthawa njuchi.
"Ndi Maliya!"
Angati atsala kuti apezeke? M'MODZI!



Kununkhira kwa zakudya za  zapadera zija  kunadzadza nyumba. Mimba ya Soniya inayamba kulira.

"Nthawi yocheka keke yafika!" anaitana amai. "Tonse tili kuyembekeza!"

Onse anayamba kuimba nyimbo ya kukondwerera tsiku la kubadwa kwa Soniya.

"Zilibwanji!"  mau okwiya anakuwa. "Musanandipeze!"



"Ndasizira Puli!" Soniya anayesetsa kuti asaseke. "Keke?" Harriet anaseka mofatsa. Zondi anaseka motseka pakamwa. "Museka bwa..." Puli anagwedeza dzanja lake lofunga. Khuthu! anagwa kuchokera mosungira zinthu mpaka pa mulu wa mapilo.



Soniya sanaseke. Anathandiza Puli kuimilira, ndi kucheka chidutswa cha keke.
"Zikomo," ananena Puli. Sanamveke kudzikuzanso. "Tsiku la bwino, Soniya."
Soniya anamwetulira. Ndi angati amene afunikira kupeza? Kulibe!



CHOTSERA!

Anzake a Soniya anai anabwera ku phwando. Pamene Jude anachoka, kunali m'modzi wochepekera pa asanu ndi anai, ndiye kuti, Anzake asanu ndi atatu. Mzake umodzi ANACHOTSEDWA pa gulu.

Tingathe kulemba motere:

(Anzake) 9 - (Jude) 1 = (Anzake otsala).



Pamene panali panatsala anzake asanu ndi m'modzi kuti apezeke, Soniya anapeza Khadani ndi Amini. Panali awiri ochepekera pa anzake asanu ndi m'modzi kuti apezeke.
Anzake awiri anachotsedwa.
Tingalembe motere:
(Anzake) 6 - (Khadani ndi Amini) 2= (Anzake otsalira) 4
Kuchotsera kwa manambala ang'onoang'ono kuchoka mumanambala akuluakulu ndiye timati KUCHOTERA KAPENA SABUTIRAKISHONI M'chingerezi.
Koma kuchotsera sikugwira nchito pochotsera anzathu okha.







Imagwira nchito kuzinthu monga njere ndi zina zilizonse...
Ngati mwachotsera njere 3 kuchotsa mwa 9, kodi zidzatsala ndi zingati?

(njere)9 -(njere)3 = ____________________(njere zotsala)

Imagwira nchito ku mangwee.
Ngati mwatenga mangwee 4 pa mulu wa mangwee 8, kodi yadzatsala yangati?

(mangwee) 8 - (mangwee) 4 =_______________________
(mangwee yatsala)

Sizodabwitsa zimenezi?

This book was made possible by Pratham Books' StoryWeaver platform. Content under Creative Commons licenses can be downloaded, translated and can even be used to create new stories - provided you give appropriate credit, and indicate if changes were made. To know more about this, and the full terms of use and attribution, please visit the following link .

Story Attribution:

This story:Ndasuzira!is translated byAgnes N.Singine Nyendwa. The © for this translation lies with Agnes N.Singine Nyendwa, 2019. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Based on Original story:'I Spy!', bySamvida Venkatesh. © Pratham Books , 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.

Images Attributions:

Cover page:Playing I Spy, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 2:Smiling birthday girl, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 3:Children celebrating a friend's birthday, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 4:Girls talking and playing hide and seek, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 5:Friends at a birthday party, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 6:A boy saying goodbye to his friends, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 7:Children playing I Spy, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 8:A girl tripping over a mat and falling down, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 9:A girl running after a dog, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 10:A girl looking behind a pile of mattresses and inside a trunk, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Disclaimer: https://www.storyweaver.org.in/terms_and_conditions

Some rights reserved. This book is CC--BY--4.0 licensed. You can copy, modify, distribute and perform the work, even for commercial purposes, all without asking permission. For full terms of use and attribution, http://creativecommons.org/licenses/by/4.0/

This book was made possible by Pratham Books' StoryWeaver platform. Content under Creative Commons licenses can be downloaded, translated and can even be used to create new stories - provided you give appropriate credit, and indicate if changes were made. To know more about this, and the full terms of use and attribution, please visit the following link .
Images Attributions:
Page 11:Two boys sitting inside a dusty cupboard, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 12:Water tank and pots, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 13: Girl finds a boy and a cat playing on the terrace, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 14:Girls running away from a bee in the garden, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 15:Children at a birthday party looking surprised, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 16:Girls offering a piece of cake to their friend, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 17:A girl giving her friend a piece of cake, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 18:A group of eight children, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 19:A group of eight children, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 20: Girl counting rajma and coins, bySandhya Prabhat© Pratham Books, 2017. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Disclaimer:https://www.storyweaver.org.in/terms_and_conditions

Some rights reserved. This book is CC--BY--4.0 licensed. You can copy, modify, distribute and perform the work, even for commercial purposes, all without asking permission. For full terms of use and attribution, http://creativecommons.org/licenses/by/4.0/

Ndasuzira! (Chinyanja)

Masewera a 'kasozo' ku phwando la kubadwa kwa Soniya yakhala yoseketsa pamene njuchi ndi chona ndi galu akhala amodzi osewera. Kodi Soniya wapeza abwezi ake onse pothera? Chotserani ndi wobadwa tsikuli kuti mudziwe zinachitika!

This is a Level 2 book for children who recognize familiar words and can read new words with help.

PRATHAM BOOKS
storyweaver

Pratham Books goes digital to weave a whole new chapter in the realm of multilingual children's stories. Knitting together children, authors, illustrators and publishers. Folding in teachers, and translators. To create a rich fabric of openly licensed multilingual stories for the children of India -- and the world. Our unique online platform, StoryWeaver, is a playground where children, parents, teachers and librarians can get creative. Come, start weaving today, and help us get a book in every child's hand!